


NDI NYUMBA YOTANI YOMWE INU MUDZANDIMANGIRA INE?

 Zikomo inu, M'bale Green. Ndi mwayi. Moni kwa M'bale ndi Mlongo Green, ndi onse omwe muli pano mmawa uno. Ndipo ndi mwayi womwe ine ndikumverera kuti ndiri nao utapatsidwa kwa ine, kuti ndibwere ku malo ano a kupembedza, kuti ndidzapanga zolengeza zingapo.

² Ine sindikufuna kuti nditenge nthawi ya M'bale Green pano, chifukwa ine ndamumvapo M'bale Green nthawi zingapo, akuyankhula, ndipo ine ndithudi ndinakopedwa, ndi momwe iye amabweretsa Mawu a Ambuye kwa ife, ndipo anali wodzichepetsa kwambiri nazo. Dzulo iye anati, “Ine sindimalandira Mawu kuchokera kwa Ambuye monga mwinamwake momwe Iwo akanamabwerera mwa vumbulutso, monga—monga Iwo akhalira akutumizidwa, koma,” anati, “Ine ndimakonda ku—kukhomerera pa zomwe zanenedwa kale.” Iye anati, “Monga pamene Paulo analemba chinachake mu Baibulo, ine ndabwera kuno kuti ndidzakhomerere pa zomwe iye ananena.” Anati, “Ine ndiribe uthenga, basi kungoti ndidzakhomerere pa zimene zanenedwa kale kuchokera kwa Ambuye.” Ine ndinaganiza icho ndithudi ndi choyamikirika, m—mnyamata wamng’ono monga uyo, ndi kumumva iye akupanga ndemanga yonga iyo.

Tsopano tiyeni tingokhala ndi mawu a pemphero limodzi.

³ Wokonedwa Mulungu, ine sindikudziwa nkomwe momwe ndingayambire, pakuti ine ndikumverera kuti Inu muli pano lero, ndipo mu Kukhalapo Kwanu ife nthawizonse timadzimverera aang’ono kwambiri. Ndipo i—ine ndikukuthokozani Inu chifukwa cha mwayi uwu. Tsopano, Ambuye, momwe Inu mwaperekera malo awa kwa ife, ife tikupemphera kuti Inu muzikomana nafe nthawi iliyonse yomwe ife tizikomana muno. Ndipo mulole Mzimu Wanu Waukulu usunthire ku mzinda uno! Mulole ife tizikhoza kuwubweretsa Uthenga wa Ulaliki uwu umene wapatsidwa kwa ife ndi kuperekedwa mmanja mwathu mu masiku otsiriza ano, mulole Iwo kuti ukwaniritsidwe, ndipo Inu mutenge solo iliyonse ya mu Tucson ndi kozungulira konse, yomwe Inu munaidzozera ku Moyo. Perekani zinthu izi, Atate, mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

⁴ Ine ndikuganiza ine ndikufuna kuti ndiwerenge ndime yaing’ono ya Lemba pano mmawa uno, basi ine ndisananene mawu awa omwe ine ndikukhumba kuti ndiwanene. Iwo

akupezeka uko mu Machitidwe, mutu wa 7 wa Bukhu la Machitidwe. Ndipo pamene inu mukutembenezira kumeneko, ife tiyambira pa ndime ya 44.

⁵ Tsopano ife tikupita ku Shreveport sabata ino, sabata ikubwera iyi, ku mndandanda wa misonkhano, ndipo tsopano ife tikayesera, ngati Ambuye alola. M'bale Moore, M'bale Jack Moore, bwenzi wabwino kwambiri wa tonse M'bale Pearry ndi ine, ndipo ife timamukonda M'bale Jack. Uthenga, ine ndikuganiza, unakhala ngati unamudodometsa iye pang'ono, makamaka pa zinthu zina zomwe ife timazigwira mokondedwa ndi kuzikhulupirira, ku—kuti Iwo unabwera kwa ife kupyolera mu kutseguka kwa Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri, monga ife tikukhulupirira Izo, monga ngati, “mbewu ya serpenti,” ndi “chitetezero Chamuyaya cha okhulupirira,” n—ndi zina zotero, ena a Mauthenga amenewo. Omwe, mwina kwa ena...Ife sitikuganiza kuti Izi ndi zovuta, koma, Iwo, iwe umayenera kuti uzitsegulira mtima wako kwa Choonadi. Ife tikukhulupirira kuti ife tikukhala mu—nthawi yotsiriza. Izo ndi zenizeni kwambiri kwa ife, kuti ife tiri basi pa mapeto a msewu.

⁶ Ndipo kuti uyankhule mu mpingo wa munthu winawake, ndiye, iwe umafuna kuti ulemekeze ulemu wa munthu ameneyo, wa—wa kukupatsa iwe mwayi umenewo kuti ubwere mu mpingo wake. Ndipo ine, ndithudi, podziwa kuti iwo samakhulupirira mu Zimenezo, ndipo ine ndikanati ndiwalemekeze iwo mokwanira kuti...Ziripo zochuluka zina zomwe ine ndingakhoze kuyankhulapo uko, pambali pa kubweretsa Izo mmenemo; kupatula ngati uli Mzimu Woyera basi ukukankhiramo Izo pang'ono, inu mukuona, ndiye ine ndithudi ndikanakhoza kunena momwe Iye wanenera. Ndipo ine sindikudziwa mwabwino mwina kuposa kuchita choncho, ndipo ine ndikuyembekeza kuti sindidzaphunzira konse mwabwinoko mwina kuposa kuchita choncho. Mwaona? Tiyeni tizingonena Izo momwe Iye akunenera Izo.

⁷ Tsopano tiyeni ife tingowerenga chabe—ndime kapena ziwiri pano kuchokera ku—mutu wa 7 wa Bukhu la Machitidwe, kuyambira ndi ndime ya 44.

Makolo athu anali nacho chihema cha umboni mu chipululu, monga iye anakonzera, polankhula kwa Mose, kuti iye achipange icho molingana ndi makonedwe omwe iye anali atawawona.

Chimene aponso makolo athu omwe anadza pambuyopo anachibweretsa umo ndi Yesu pa kutenga za Amitundu, anene Mulungu anawaingitsa patsogolo pa nkhope za makolo athu, mpaka ku masiku a Davide;

Yemwe anapeza chisomo pamaso pa Mulungu, ndipo anakhumba kuti ampezere kachisi Mulungu wa Yakobo.

Koma Solomoni anamumangira iye nyumba.

Ngakhale ziri choncho Wammwamba kwambiriyu samakhala mu nyumba zomangidwa ndi manja; monga anena mneneri.

Kumwamba ndi mpandowachifumu wanga, . . . dziko lapansi ndi choponderapo mapazi anga: ndi nyumba yotani yomwe inu mudzandimangira ine: atero Ambuye: kapena malo a mpumulo wanga ndi chiani?

Kodi manja anga sanapange zinthu zonse izi?

⁸ Pa Izi, kuwerenga kwa Lemba ili, ine ndikufuna kuti ndinene mawu pang'ono omwe ine ndikufuna kuti ndiwanene M'bale Pearry asanabweretse uthenga wa mmawawu.

⁹ Ine ndikupeza ino imodzi ya mphindi zanga zazikulu za kudzacheza kwanga ku Tucson. Ine ndinabwera kuno chifukwa chakuti ine ndinatsogozedwa kuti ndibwere kuno. Ine ndinabwera kuno chifukwa chakuti Mzimu Woyera, kupyolera mu masomphenya, unanditumiza ine kuno. Ine ndikudziwa izo zikhoza kuwoneka zachilendo, mwinamwake. Koma Iye, monga momwe ine ndikudziwira, chirichonse chimene ine ndikuchidziwa cha Mulungu, ine ndinatuzidwa mwa masomphenya ku Tucson. Ine ndakhala ndikudabwa momwe ine ndikutuzidwira konse ku malo achipululu awa. Ndiyeno kuno kumene kuli . . .

¹⁰ Kuyankhula mwauzimu, pa mzindawu, ine sindikudziwa malo ena omwe ali akufa mwauzimu kwina mochulukira, kuposa mu mzinda wa Tucson. Muli nkondo pakati pa mipingo. Muli makangano pakati pa osonkhana. Mulibe chiyanjano ayi, ndipo aliyense akumaphangira, ndi kugwirizitsa, ndi kufinya, ndi kuyesera kuti amutenge wina *uyu*, ndi kubelana. Ichi ndi chipululu, kuyankhula mwauzimu, naponso.

¹¹ Komano ine ndimawerenga mu Baibulo, kuti pamene Mulungu anamuitana Mose kuti achoke kwa okonedwa ake ndi onse omwe anali okonedwa kwa iye, ndi kumutumiza iye ku chipululu, kuti akalembe Malamulo a Baibulo. Icho chinali Chipangano Chakale, Mabuku anai oyambirira, Genesis, Levitiko, ndi Deteronome, Eksodo. Iye . . . ine sindinawatchule konse iwo basi mwa mndandanda, koma ndiwo Mabuku anaiwo. Awo ndiwo kwenikweni ali Chipangano Chakale. Chifukwa, ena onse a Ilo anali zomwe aneneri ankanena, mu Masalmo a Davide, ndi zina zotero, koma Mbiri ya mafumu. Koma awa anali chikhazikitso cha Chipangano Chakale. Anali Mose anawalemba iwo iye ataitanidwa kale kuchokera ku dziko lakwawo, kumene iye anabadwirako ndipo analeredwa pakati pa abale ake, ndipo anatuzidwa ku chipululu, kuti akalembe Bukhu ili la Chipangano Chakale.

¹² Ndiye ine ndikupeza kuti mu Bukhu la Chipangano Chatsopano, pamene Paulo, yemwe ali mwini, kapena osati mwini, koma mlembi wa Chipangano Chatsopano. Iye aponso

anachotsedwa pakati pa abale ake, ndipo, mwa Mzimu, anapita ku Arabia, kumene Iye anakakhala zaka zitatu ndi theka, kuti akapeze kudzoza. Ndipo Paulo ndi mlembi wamkulu wa Chipangano Chatsopano. Tsopano, pali Mateyu, Marko, Luka, ndi Yohane, koma iwo anali alembi omwe ankangolemba zomwe Yesu ankanena pamene iwo ankamutsatira Iye limodzi. Ndipo, koma, inu mukatenga Bukhu la kwa Timoteo, ndi kwa Aroma, ndi kwa Ahebri, ndi ena otero, Paulo analandira kudzoza kuti alembe Chipangano Chatsopano; kutenga Chipangano Chakale chonse ngati mthunzi, ndi kuziika izo mu dongosolo. Ndipo Mulungu anazilemekeza izo, ndipo anachipanga icho kukhala Chipangano Chatsopano.

¹³ Ndipo tsopano ngati Chipangano Chakale anachita kutsogozedwa kuchokera...mlembiyo anachita kutsogozedwa kuchokera kwa abale ake, kupita mu chipululu, kuti akapeze kudzoza koti alembe nako Chipangano Chakale. Ndipo mu Chipangano Chatsopano, mlembiyo anatsogozedwa ndi Mwini, kupita ku malo achipululu, kuti akapeze kudzoza kuti alembe Chipangano Chatsopano. Ndipo Mabukuwo ali osindikizidwa ndi Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri; iwo nawonso angasowe mofanana, ine ndikukhulupirira, mu masiku ano, kuti atsegule Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri izo. Kuti usiye zomwe iwe umazigwira mokondeka, ku zomwe iwe umazisamalira, ndi nyumba yaing'ono yomwe inapatsidwa kwa ine ndi anthu, ndi pakati pa abale anga onse ndi amzanga, ndi mpingo womwe unali kuyanga, ndipo unalibe kanthu kena kosowa; ndipo ku—kuti uzisiye izo, kuchoka kumene kwa izo, ndi kupita kutali, kupita mu chipululu kumene iwe sumamudziwa aliyense, ndipo chirichonse chikukutsutsa iwe.

¹⁴ Koma pali chinachake ndi Mulungu, kuti Iye amamutsogoza munthu kuti azichita zinthu zomwe ziri zopitirira kuganiza kwake kwake kulikonse, kotero kuti izo zikhoze kukhala kwa ulemero ndi ulemu wa Mulungu. Ndipo ine ndikumverera kuti, osati ulemu wawekha, koma i—ine ndikumverera kuti iwo unali mwayi kusiya chirichonse chimene chinkatchedwa chofunika kwa ine, kuti ndibwere kuno mu chipululu ichi ndi kudzavutika monga ine sindinayambe ndavutikapo mu moyo wanga, kuno mu nkhalango ino, kapena chipululu ichi. Koma ine ndikukhulupirira, kuti pa kuchita izo ndi kumvera zomwe Mulungu analamulira kuti zichitidwe, Mulungu watsegulira kwa ife zinsinsi za tsiku lotsiriza lino. Ndipo ife tiri pano ndi Uthenga uwu.

¹⁵ Tsopano, panali anthu ochuluka omwe ananditsatira ine, ndipo izo si zosazolowereka. Kawirikawiri munthu ife... Anthu amakondana wina ndi mzake, ndipo icho, chikondi, chimakutsogoza iwe kuti uchite zinthu zomwe sumaganiza kuti ukanazichita. Ndipo ambiri a inu mwasiya makwanu,

inu mwasiya zonse, kungoti mupite, mubwere kunja kuno mu chipululu.

¹⁶ Ambiri andiyimbira ine, ambiri andifunsa ine, “Kodi ife tibwere ku Arizona? Kodi iwo akakhala malo abwino kwa ife?” Chabwino, monga izo zinanenedwa kwa Mose ndi iwo, ajawa anali malo opanda chipatso, iwo sanali malo a manyumwa.

¹⁷ Kuno kulibe ntchito zambiri zoti nkuchita, ndipo moyo ndi wodula, ndipo mtengo wa kukhala moyo ndi wodula. Ndi malo ovuta kwenikweni kuti uzikhalako, mu Tucson, Arizona; malipiro ndi operewera, ndi—ndipo chakudya ndi chodula, ndi rendi. N—ndi malo oyipa kuti uzikhalako, mu chikhalidwe chimenecho. Koma ndi kwathanzi, ndi kowuma. Ndipo ife nthawizina . . . Ife tisamafikitse malingalira athu mu kachitidwe ka zinthu za dziko lapansi.

¹⁸ Ife tiyenera kuti tiziyang’ana ku kutsogolera kwa Mzimu Woyera. Koma chinthu chimodzi chimene chimandisautsa ine pamene ndimabwera kuno, ndi kuwauza anthu, chabwino, “inu musabwere” kapena “inu mubwere,” izo ine ndazisiyira kwa aliyense payekha, momwe Mulungu akumutsogolera payekha uyo kuti achitire. Ine ndikuganiza aliyense wa ife azichita zimenezo, azitsogozedwa ndi Mzimu, pa zoti achite.

¹⁹ Ndipo ambiri a inu pano ndinu ochokera kozungulira Jeffersonville, ndi a osonkhana a kumeneko, ndipo inu mwabwera kuno. Tsopano, chinthu chimene chimandisautsa ine, chinali malo opembezako.

²⁰ Ndipo ine ndikuzindikira, pamene ine ndimawerenga mu Lemba pano, za Stefano ndi zoyankhula zake isanachitike kumene imfa yake; pakuti iwo anamugenda iye mwamsanga pambuyo pake, chifukwa cha uthenga wake. Pamene iye anali kuyankhula, iye anati, “makolo athu,” kuyankhula za Ahebri mu tsiku loyambiriralo, momwe iwo anayesera kuti apeze chifundo pamaso pa Mulungu, kuti amange malo opembezderapo. Iye ananena kuti, “Solomoni anamumangira Iye nyumba, kapena chimango.” Ife tikuidziwa nkhaniyo.

²¹ Koma ine ndimawakonda mawu ake otsatirawa, “Ngakhale ziri choncho Wammwamba kwambiriyo samakhala mu nyumba zomangidwa ndi manja,” ndipo mu malo ena uko mu Yesaya. Iye anati, “Thupi Inu mwandikonzera Ine; onani, nsembe ndi zopereka, ndi nyumba, ndi zina zotero, koma thupi Inu mwandikonzera Ine.” Chabwino, ife tikuzindikira kuti iye anali kuyankhula apo za thupi mmene Mulungu anadzakhalamo, mwa Khristu.

²² Koma ine ndikukhulupirira lero, kuti kudzoza kwabwera kwa—kwa M’bale Green, kuti asamukire kuno, iye ndi Mlango Green, kusiya malo awo uko kummawa, nawonso, limodzi, komwe uko ku Texas, kuti abwere kuno ndi kudzayamba opanda kanthu; mophweka basi mwa kudzoza, atamverera

kuti iwo ayenera kuchita izo. Ine ndimayamikira amuna omwe angatsatire kutsogolera kwa Khristu, mosasamala mtengo womwe zingawatengere iwo.

²³ Ngakhale dziko lonse, mwinamwake abwenzi ako kwambiri, angaganize kuti iwe ukulakwitsa, koma izo sizolakwitsa kwa iwe. Bola ngati ukumverera kuti pali chinachake kumbuyo kwa izo, ndi Mulungu akukuyendetsa iwe; izo siziri konse zolakwika, ndipo izo nthawizonse zimathera kukhala molondola.

²⁴ Kuwaona banja laling'ono ili, mnyamata walunthayu. Ine sindikunena izi chifukwa iye ali pano. Ndi dona wamng'ono uyu ndi ana ake, ndi banja lake loti alilere, ndipo iye wasiya ntchito yake ndi chirichonse, kuti asamukire kuno.

²⁵ Ine ndikuzindikira kuti zaka zapitazo ine ndinaitanidwa mu utumiki. Ine sindinakhalepo m'busa wochita bwino, chifukwa ine ndiri ndi mzimu woyendayenda, wosakhazikika. Ine sindingakhutitsidwe kulikonse. Basi kulikonse kumene Mzimu upita, ine ndimayenera ndizipita ndi Iwo, chifukwa ine ndiri ndi Uthenga. Yesu anati, "Ine ndiyenera ndikalalikire mu mzinda wina uwunso."

²⁶ Koma alipo awo omwe ali abusa omwe amaziyang'anira nkhusa. Ndine woyamikira kwambiri kuti M'bale Peary anatsatira kutsogolera kwa Mzimu Woyera, ndipo lero ife tiri ndi kachisi. Iye ndi wamng'ono. Uyu ndi wabwino basi kuti tiyambire naye, kuti tiwone chimene Mzimu Woyera... Mopanda kudziwa, tiyeni tizingosuntha phazi ndi phazi. Tsopano, ine ndikukhulupirira, ngati Mulungu wayankhula kwa M'bale ndi Mlongo Green, kuti abwere kuno, ndipo wategula malo kumene ana athu; mmalo mwa Lamlungu mmawa kumakwera njira zawo, ndi pa misewu akuthamanga thamanga, iwo ali nawo malo oti azibwera kudzapembedzako, mmalo moti ife tizingokhala ndi kumamvetsera kwa chinachake chimene ife tachimva pa walesi, zomwe ziri zabwino.

²⁷ Koma ife, ngati gulu lino la anthu, ife tiri ndi Uthenga wa tsiku lino. Ife, ife tikukhulupirira kuti Mulungu watipatsa ife Uthenga. Ndipo M'bale Green, ali, ine sindikufuna kuti ndimutche iye wothandizana naye wanga, chifukwa ife tiri... Chabwino, nzomwe ziri, naponso, wothandizana naye wanga, ife tiri limodzi mu Uthenga uwu. M'bale Green amalalikira chinthu chomwecho ndi Uthenga umene ine ndimaukhulupirirawu. Iye anachoka kwawo, anawasiya abale ake, anawasiya mpingo wake. Iye anali, ine ndikukhulupirira, iye anali woyang'anira mzinda kapena chinachake, wa limodzi la mabungwe, ndipo anachisiya chinthu chonsecho pamene iye anaumva Uwu. Iye anasiya chirichonse chimene chinali chokondeka kwa iye, ndiponso, kuti abwere ku chipululuchi, basi kuti azidzathandizira chimene Mulungu akupereka kwa ife tsopano.

28 Ine ndikuti ine ndikukhulupirira izo sikuti zizikhala mu mtima mwathu mokha, iyo iyenera kuti izikhala ntchito yathu kumamuimira iye kumbuyo, chirichonse chimene ife tingakhoze, kukhala nawo pa misonkhano, kumabwera kuno kudzapembedza, ndi kuwapanga ano malo kumene Mulungu angakhoze kumawulula kwa ife zinthu zomwe Iye ali nazo kwa ife kuti aziwulule. Ndipo monga mawu ake anati, “Uthenga sumabwera kwa ine kupyolera mu kupereka kwa kudzoza, monga iwo umachitira mwinamwake kwa ena a ife, koma,” iye anati, “Ine ndiri pano kuti ndiziimira kumbuyo zomwe Mulungu wapereka.” Ndi neno bwanji! Ndipo ine ndikukhulupirira, ngati ife tonse tingagwirizane limodzi, ife tiika mitima yathu kwa iwo.

29 Ine ndikudziwa kuti aliyense wa inu, ngati inu mukumverera monga ine ndikuchitira, ndine wanjala kwambiri kuti ndiwuwone Mzimu wa Mulungu ukuyenda, ine basi sindingakhoze kupirira nazo nkomwe. Zondichitikira zina zomwe ine ndinali nazo uko ku phiri, kuti ndingomverera izo kamodzi kenanso, Chinachake chija chimene pamene ine ndinapulumutsidwa koyamba chomwe chinali chaulemerero kwambiri kwa mtima wanga! Ndipo ife tikukhoza kubwera mu malo, ife tikukhoza kukhala ndi kumaziwona izo pakati pathu, kuti ife tikuwuma. Pamene ife tikukhala kuno mu chipululu, ine ndimafika pakati pa abale anga, iwo amayankhula ndi ine ndipo ine ndimayankhula ndi iwo; nthawizonse, mwanjira yaing’ono yopenyesetsa, kumverera kunja uko ndi Mzimu, momwe ziriri, kuti ndingowona chikhalidwe cha m’bale ameneyo, kuti ndiwone zomwe ziri zolakwika. Ine ndimayamba kumverera kuti izo zonse zikupendeka, zikuchoka ku Mzimu. Izo zikusanduka chinthu chachibadwa kwambiri kwa ife. Ife tiyenera kuti tizipembedza mu Mzimu, kumene Mzimu wa Mulungu. . . Osati kuti Uthenga wathu uzikhala kokha lawi la orali, iwo uyenera uzikhala lawi la mu mtima mwathu. Mukuona? Iwo uyenera uzikhala uli mu mitima yathu, kapena ife sitingakhoze—ife sitingakhoze kuwupereka Iwo molondola kwa anthu. Mzimu uyenera uzinyamula Uthenga, Iwowokha. Ndipo ine ndikudalira ndi kukhulupirira mwa aliyense wa inu, kuti mukhala Mkristu weniweni.

30 Tsopano iwo akusowa aphunzitsi a Sande sukulu. Iwo asowa antchito. Ndipo ine ndafuna kuti ndinene izi kuti inu mumvetse kwathunthu. Ichi ndi tchalitchi changa.

31 Ine ndakhala ndiri kuno zaka zitatu. Ndipo ine ndinali ndi khomo limodzi lotsegukira kwa ine, limenelo anali M’bale Mack anandipempha ine kuti ndibwere ndidzalalike. Mulungu amudalitse iye. Ine sindinaitanidwe ndi anthu ena aliwonse; ndiribe chirichonse chotsutsana ndi iwo, iwo ndi abwino bwino. M’bale Brock, bwenzi labwino la ine, M’bale Gilmore, ambiri a abale Achipentekoste awa kuno, ali kwambiri mbiri, abwenzi abwino mwakuya kwambiri a ine. Ine ndimawakonda iwo;

ndiribe kanthu kowatsutsa iwo. Ine ndikumvetsa pomwe ali. Iwo sangakhoze kundiitanira ine kumeneko, ndipo iwo nkutsalirabe mu bungwe lawo. Mwaona, iwo sangakhoze kuchita izo. Chifukwa, ngati iwo atero, iwo athamangitsidwira kunja. Kotero iwe ukuona pomwe ali. Ine ndinali nacho chinthu chomwecho chimene ndinakomana nacho. Koma tsopano lolani nthawizonse zizikhala ziri, “Funani inu poyamba Ufumu wa Mulungu,” chifuniro cha Mulungu.

³² Ndipo tsopano poti, M'bale Green, Mulungu wamutumiza iye kuno ndipo watitsegulira ife mpingo wa Chikhulupiriro chofanana chofunika chimene ife tiri kukhulupiriramo, ife tiyenera kukhala oyamikira kwambiri kwa Mulungu, ndi kumakhalapo pa msonkhano uliwonse, tizitenga malo aliwonse omwe ife tingathe. Ndipo ngati ife tifunsidwa ndi kuitanidwa, kuti tipemphere, kuti tifunefune, kuti tichite, tiyeni tikhale asilikari okhala pa...ofunitsitsa basi kuti tizichite izo. Mwaona?

³³ Usungeni Uthengawu mwaulemu, ndipo muzikhala moyo wa mtundu wolondola. Musati mulole mwaye ubwere pa Iwo. Ife tikukhala mochedwa kwambiri tsopano. Ife tiri—ife tachedwa kwambiri mu orali. Tiyeni tiwukhale Iwo mwachiyero. Kapena, moyo wanga, moyo wanu, miyoyo yathu yonse ikusowa kuti inyamulidwire mmwamba, pamaso pa Mulungu.

³⁴ Anthu athu achichepere amangokwera nazungulira, kuchokera ku malo kupita ku malo, kuchoka ku chiwonetsero kupita ku chiwonetsero, ndi kumaseserekerera kutali ndi motalikira kwambiri ndi Mulungu. Uko nkulondola. Tsopano, izo ndi zoonza. Ine ndimaziwona izo mwa ana anga, ndipo ine ndikudziwona inemwini ndikufika pa malo omwe osati... Inu, inu tikuyenera kumadzisonkhanitsa tokha palimodzi, kuti tizimupembedza Mulungu; Baibulo linanena chomwecho, “Pamene ife tikuliwona tsiku ili likuyandikira, mochuluka kwambiri chotero tizibwera palimodzi.” Ngati pali anthu awiri okha pano, inu mukhale mmodzi wa iwo. Tsopano ndizo... Ndipo ngati ife tibwera palimodzi ndi kumapembedza limodzi, ndiye ife basi, chinthu china chimzake cha izo, Yesu anati, “Pamene awiri kapena atatu asonkhana mu Dzina Langa, pamenepo ine ndiri pakati pawo.”

³⁵ Tsopano, monga ine ndimanena poyamba, M'bale Green anandiuza ine, ndipo iye ananena izo. Akazi anga anabwera, anadzandiuza ine zomwe iye amanena pamene ine ndinali nditachokapo. Izo, ndipo iye wazinena mmawa uno, kuti, “Guwa ndi lotsegula nthawi iliyonse.” Tsopano kawirikawiri...Kuti, nlotseguka kuti ine ndiziyankhulapo.

³⁶ Tsopano, kawirikawiri, ine ndimachita kuyendetsa njira yonse mpaka ku Jeffersonville, Indiana, kuti ndikapereke Uthenga umene Mulungu wandipatsa ine, kuti ndikawubweretse

iwo kwa anthu; ndimapita ulendo wonse mpaka ku Jeffersonville, Indiana, ndipo aliyense wa inu mukulumikiza kudutsa dzikoli, ndi kulumikiza mawaya ndi zinthu, kuti mumvetsere Uthenga, chifukwa ndi chimene ife tikukhalirapo moyo. Mukuona, ndi chomwe ife takhalira kuno. Chabwino, ife sitikusowa kuti tizichita izo kenanso.

³⁷ Mulungu akandipatsa ine Uthenga, ine ndizikhoza kuyenda kumka pa guwa pomwe pano ndi kudzaulalikira iwo, ndi kumverera womasuka pakuchita izo. Mwaona? Ndipo ine ndikukhulupirira, pa kutero, kuti Mulungu Wamphamvuzonse akudalitsani inu ngati inu muti mungoima nacho tchalitchi ichi tsopano, gulu lino la anthu. Osati izo zokha, koma tiyeni tizipita kunja ndi kukawona ngati sitingakhoze kukawapeza ena oti abwere muno. Mukuona, tiyeni tiziyankhula kwa enanso kulikonse, tiziyankhula kwa iwo za tchalitchi chathu ndi chomwe icho chikutanthauza. Chimene tchalitchi chathu. . . Ife tiri pano. Ife tikufuna kuti inu muzibwera, zibweretsani muno alendo, ndipo ine ndikutsimikiza zizikhala zabwino kwa tonse ife. Mwaona? Ife tiri ndi nyumba, yomwe ife tiri othokoza nayo. Ndife othokoza chifukwa cha malo ano, kuti tizisonkhanamo palimodzi.

³⁸ Koma, “Ngakhale ziri choncho Wammwamba kwambiriyo samakhala mmakachisi omangidwa ndi manja, mwaona ‘Pakuti Kumwamba ndi mpandowachifumu Wanga, ndipo dziko lapansi ndi popondapo phazi Langa; ndipo alikuti malo a mpumulo Wanga? Koma thupi Inu mwandikonzera Ine.’”

³⁹ Ndipo ife ndife Thupi la Khristu. Kotero pamene ife tikusuntha kuchokera ku nyumba ina kupita ku nyumba imzake, ine ndikukhulupirira, pobweretsa Mauthenga athu, ndipo ife tizibwera kuno ndi kudzakhala ndi misonkhano ya machiritso. Ndipo chirichonse chimene Ambuye azichiwululira kwa ife kuti tizichita, ife tizikhala nazo izo momwe muno mu tchalitchi, mpaka iwo utafufuma mokula kwambiri mpaka inu mudzayenera kudzawutengera iwo kwina kwake, ndi kwina kwakenso, mpaka Yesu atadza. Mulungu akudalitseni inu.

⁴⁰ [M’bale Pearry Green akuchitira ndemanga, ndiyeno akumupempha M’bale Branham kuti amudzoze iye—Mkonzi.]

Tiweramitse mitu yathu.

⁴¹ Wokonedwa Mulungu, pamene ife taima pa nsanja ino, yomwe ikuimira, pa guwa pomwe pano, ife tikuzindikira kuti ife tiri—mtundu wakufa wa anthu, momwe dziko lino limachitira. Ife timayang’ana kunja pa misewu ndi kuwona tchimo litalembedwa paliponse, ndi kuti Ulemerero wa Ambuye ukuchoka mwaliwiro. Ndipo ife tikudziwa, pamene Ulemerero wa Ambuye ukukwera mmwamba, chomwecho Mpingo upita nawo Iwo. Mulungu, ife tikufuna kuti tikakhale kumeneko.

⁴² Masiku pang'ono okha apitawo, nditaima kuno pa ngodya ya msewu, patsidya pa msewu pomwepa, ndikuonera perete uja akupita mmusi ndi msewu; ndi kuziwona zimathanki za Nkhondo Yoyamba ya Dziko lonse zikutsogolera njira, ndiye kunabwera thanki yaikulu yolemera ya chi Sherman, kumbuyo kwa iyo motsatira akupita pang'ono ndi pang'ono, kenako amayi a nyenyezi-yagolide; banja laling'ono losweka, ndi mkazi wolira, ndi mnyamata wamng'ono wasanza atataya bambo ake, amayi achikulire anali atataya mwana wao. O, kukwiyitsa kwake kukhala utaima pa ngodya ya msewu ndi kumaonera chinachake chonga icho chikudutsa! Ndiye nkuzindikira, basi pamene iwo ankadutsa pa nyumba ino, nyimbo inasintha nkukhala "Patsogolo, Asilikari Achikhristu." Kusewera mwa kuguba kwawo, mmbuyomo; koma npamene iwo ankadutsa pa malo ano!

⁴³ Wokonedwa Mulungu, ine ndikuganiza za nthawi ina yaikulu ikudza, ndipo iyo idzakhala chiukitsiro, pamene anthawi-zakale adzatulukira poyamba, oyera, mbadwa. "Pakuti ife omwe tiri moyo ndipo tatsalira sitidzawalepheretsa kapena kuwatsekereza iwo omwe ali chigonere; pakuti lipenga la Mulungu lidzawomba, ndipo akufa mwa Khristu adzauka choyamba." Ndiye pamene ife tidzawona aakulu awo... anthu awo basi akupita, akuguba chokwera kudutsa mlengalenga; ndipo ife tidzakhala titaima, tikuyembekezera kusintha kwathu, tikudziwa kuti ife tigwera mu mzere, nafenso. Mulungu, tipangeni ife kukhala asilikari okhulupirika.

⁴⁴ Iwo okha omwe tayanjana nao kwenikweni ndipo akhala ali mu nkhondoyi adzadziwa chomwe izo zinkatanthauza kwenikweni, powawona mathanki aja akugudubuzika chodutsa. Ndipo, Mulungu, ife tikuganiza kuti iwo omwe akhala ali mu nkhondo ya moyo adzadziwa chimene izo zikutanthauza, pamene ife tikuyembekezera nthawi yathu kuti tigwere mu udindo ndi pamalo, mu chiukitsiro, kuti tizipita mmwamba.

⁴⁵ Ndipo uyu, m'bale wanga wamng'ono, waima apayu, ataphunzitsidwa bwino, wakonzeka, wavekedwa, akuyembekezera mwamuna wachikulire kuti ayike manja pa iye, yemwe ali wankhondo wakale amene wakhalako kutsogolo kwa mzere uko, podziwa kuti iye ayenera kuti alowe mu nkhondo, nafenso. Wokonedwa Mulungu, ndi manja osayenera awa ine ndikuwasanjika pa m'bale wanga, mwa kuimira kwa Anu. Mdalitseni M'bale Green, wokonedwa Mulungu, yemwe ine ndikumudalitsa mu Dzina la Yesu. Mulole iye awunyamule Uthenga uwu, Ambuye, apite nawo mu mzinda uno ndi kulikonse komwe Inu muti mumuitanire iye. Mulole iye akakhale womvera, wodzazidwa ndi Mzimu, akukhala moyo wapamwamba pa chitonzo. Mulungu, mumulole iye akhale nayo mitima ya anthu, kuti iye akhoze kumawaphunzitsa iwo ndi kuwatsogolera iwo

ndi kuwalondolera iwo mu njira yomwe ife tonse tikukhumba kuti tiziyendamo. Perekani izi, Ambuye.

⁴⁶ Mudalitseni mkazi wake wokhulupirika, ana ake aang'ono. Mudalitse kuyesetsa kwathu pano palimodzi, monga abale Achikhristu kuno padziko lapansi, kuti ife tikhoze kuwutengera Uthenga uwu ku mathero a dziko. Mutumize Mzimu Wanu pa iye, Mulungu. Ife tikupemphera mu Dzina la Yesu Khristu, pamene ife tikumupereka iye kwa Inu. Ameni.

Mulungu akudalitseni inu, M'bale Pearry. Zinyamulani Mawu a Mulungu!



NDI NYUMBA YOTANI YOMWE INU MUDZANDIMANGIRA INE? CHA65-1121
(What House Will You Build Me?)

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham woperekedwa mu Chingerezi Lamlungu mmawa, Novembala 21, 1965, ku Tucson Tabernacle mu Tucson, Arizona, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kumasulira uku kwa Chichewa kunadindidwa m'chaka cha 2003 ndi Voice of God Recordings:

CHICHEWA

©2012 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org